

UFULU WA ALIMI





Olemba:

Juanita Chaves Posada - Global Forum on Agricultural Research

Ounika:

Teshome Hunduma - Development Fund of Norway, William Chadza- Centre for Environmental Policy and Advocacy

Komiti younikanso:

Agatha Chimsewa (Centre for Environmental Policy and Advocacy)
 Dr Godwin Mkamanga (biodiversity Conservation Initiative)
 John Chipeta (National Association of Smallholder Farmers)
 Nolipher Mponya (Malawi Plant Genetic Resources Centre)
 Mahara Nyirenda (Development Fund of Norway)
 Precious Chizonda (Food and Agriculture Organisation)



©2016. GFAR, Development Fund of Norway and CEPA.

Bukhuli likhoza kutsindikizidwanso bola kuonetsa kuti iyi ndi ntchito ya GFAR, Development Fund Norway ndi CEPA.



Zakudya zosiyanasiyana zomwe alimi amadya mu boma Rumphi.

CONTENTS

MUTU WOYAMBA: CHIYAMBI CHA UFULU WA ALIMI M'MALAWI.....	6
Kodi Ufulu Wa Alimi Utanthauzanji?.....	6
Ufulu Wa Alimi Uli M'magawo Awa.....	6
Zomera Zosiyanasiyana za M'dziko la Malawi.....	8
Kodi Ufulu wa Alimi Ungakwaniritsidwe Bwanji?.....	9
Njira Zotetezera Mbewu ndi Zomera Zam'ntchire.....	10
Njira Zolimbikitsira Ufulu wa Alimi, Komanso Ntchito Yosunga ndi Kuteteza Mbewu M'minda Yawo.....	10
Njira Zokwaniritsira Ufulu wa Alimi Wosinthanitsa, Komanso Kugulitsa Mbewu Zochokera M'minda Mwawo.....	15
Njira Zothandiza Kukwaniritsa Ufulu wa Alimi Wotenga Nawo Gawo pa Zokambirana Makamaka pa Nkhani Yosunga ndi Kugwiritsa Ntchito Moyenera Mbewu.....	18
Njira Zabwino Zokhazikitsira Ufulu wa Alimi Woteteza Nzeru, Luntha ndi Njira za Makolo Zosungira ndi Kugwiritsira Ntchito Mbewu Moyenera.....	19
Maganizo Otsiriza ndi Mavuto Ofunika Kuthana Nawo.....	22
MUTU WACHIWIRI: MALO OSUNGIRA MBEWU A KUMUDZI	23
Kukhala ndi Malo Osungira Mbewu M'madera a Kumudzi Kumathandiza Kulimbikitsa Ufulu wa Alimi.....	24
Eni Malo Osungira Mbewu ndi Magulu a Alimi a Kumudzi Akukwaniritsa Ufulu Wawo Motere.....	24
Zoti Atsogoleri Atsate Pokhazikitsa Kapena Kuthandiza Malo Osungira Mbewu Kumudzi.....	24
MUTU WACHITATU: UFULU WA ALIMI ACHIZIMAYI	26
Udindo wa Amayi pa Ulimi.....	26



MUTU WOYAMBA

CHIYAMBI CHA UFULU WA ALIMI M'MALAWI

Mgwirizano wa pa dziko lonse woona za mbewu zomwe zimapereka chakudya pa ulimi wa International Treaty on Plant Genetic Resources for Food and Agriculture womwe udakhazikitsidwa m'chaka cha 2001 ndipo udayamba kugwira ntchito yake m'chaka cha 2014 ndiwokhawo womwe umavomereza poyera za ufulu wa alimi. Ntchito yomwe alimi akhala akugwira m'maiko mwawo-makamaka m'madera momwe mitundu ya mbewu zosiyanasiyana idayambira, kutetezedwa, komanso kusungidwa-ndiwo maziko enieni a ufulu wa alimi. Alimi ang'onoang'ono akhala akugwira ntchito yotamandika yotukula ulimi, komanso kulimbana ndi njala makamaka m'maiko omwe akukwera kumene posunga mitundu ya mbewu zosiyanasiyana ngati mbali imodzi.

6

Malawi ndi dziko lalikulu mahekita 11.8 miliyoni. Nyanja ya Malawi ikupanga gawo limodzi la magawo asanu a dzikoli. Mwa mahekita 11.8 miliyoni omwe apanga dzikoli, mahekita 9.4 miliyoni ali ndi nthaka yoyenera ulimi. Chuma cha dziko la Malawi chagona pa ulimi. Mwa anthu 100 aliwonse a m'dzikoli, 85 amakhala m'madera akumudzi. Anthu 2.67 miliyoni mwa anthu pafupifupi 15 miliyoni omwe ali m'dziko la Malawi ndi alimi ang'onoang'ono. Ngakhale anthuwa ndi alimi ang'onoang'ono, amalima mbewu zomwe zimapereka chakudya kwa anthu 80 mwa 100 aliwonse wokhala m'dzikoli. Mwa magawo 100 a chuma chomwe dziko la Malawi limapeza kuchokera ku ulimi, alimi ang'onoang'onowa ndiwo amapanga magawo 70. Potengera chuma chonse cha dziko lino, magawo 39 a chumacho amachokera ku ulimi omwe amachita alimi ang'onoang'onowa.

Malingana ndi mgwirizano wa maiko onse, ufulu wa alimi uyenera kulemekezedwa, komanso kulimbikitsidwa ndipo udindo wokwaniritsa izi, uli m'manja mwa maiko awo.

KODI UFULU WA ALIMI UTANTHAUZANJI?

Ufulu ndi zomuyenereza munthu kukhala nazo posatengera kuti ndi wa mwamuna kapena wamkazi, mtundu wake, komwe amachokera, chipembedzo chake, chilankhulo chake ndi zinthu zina zomwe zimasiyanitsa anthu pachikhalidwe kapena pachuma. Ufuluwu umakhudzana kwambiri ndi kayendetsedwe ka boma, ndale, chuma, chikhalidwe, komanso mmene magulu a anthu ayenera kukhalira.

UFULU WA ALIMI ULI M'MAGAWO AWA:

- (i) Kusungu mbewu: Ufuluwu ukuphatikizirapo wosamalira chilengedwe ndi malo womwe chimapezekamo. Alimi ang'onoang'ono amagwira ntchito yotamandika yoteteza, kusungu ndi kusamalira mbewu ndi chilengedwe. Izi zimathandiza kuchepetsa mavuto wodza ndi kuwonongeka kwa chilengedwe, matenda ndi tizilombo towononga mbewu. Iyi ndi imodzi mwa njira zabwino zotetezera nzeru zomwe makolo akhala akugwiritsa ntchito polimbana ndi njala kwa nthawi yayitali.

Mgwirizano wa padziko lonse woona mbewu zomwe zimapereka chakudya pa ulimi wa International Treaty on Plant Genetic Resources for Food and Agriculture udazindikira ndi kuvomereza ntchito yotamandika yomwe alimi ang'onoang'ono amagwira posamalira ndi kusungu mbewu. Mabanki a mbewu akumudzi ndi imodzi mwa njira zomwe amagwiritsa ntchito posunga mbewuzo.

- (ii) Kugwiritsa ntchito mbewu zawo: Izi zikugwirizana kwambiri ndi ntchito yosungu ndondomeko yothandiza alimi ang'onoang'ono kudzipezera zosowa zawo za tsiku ndi tsiku. Alimi ang'onoang'ono ali ndi ufulu wobzala mbewu zawo zaka zingapo pofuna kugonjetsa njala, kupititsa patsogolo



Mlimi wachitsanzo Juliet Lungu ndi mwamuna wao kuonetsa kalozera mmunda mwao yemwe amathandiza kusunga madzi m'munda omwe amathandiza makamaka munthawi yosowa mvula.

miyoyo yawo, komanso kudzipazera zosowa zawo. Mabungwe ndi makampani ena ali ndi mbewu zawo za makono zomwe salola alimi kuzigwiritsa ntchito mmene akufunira.

Ufulu wa alimi wogwiritsa ntchito mbewu zosiyanasiyana umaphatikizirapo wobzala mbewu za makolo, komanso zomwe zili pachiopsezo choyiwalika kapena kutha.

- (iii) Kusinthanitsa mbewu zawo: Alimi ali ndi ufulu wosinthanitsa mbewu zawo monga momwe akhala akuchitira zaka zambiri zapitazo. Mchitidwe wosinthanitsa mbewu ufotokozedwa bwino kutsogoloku.
- (iv) Kugulitsa mbewu zomwe amalima: Alimi ang'onoang'o ali ndi ufulu wogulitsa mbewu zawo. Ngakhale izi zili choncho, maiko ayenera kukhazikitsa malamulo wovomereza ndi kulimbikitsa

mchitidwewu.

- (v) Kutenga nawo gawo pa zokambirana, komanso kumanga mfundo zokhudza kusunga ndi kuteteza mbewu: Alimi ang'onoang'ono ali ndi ufulu wopanga nawo ziganizo zokhudza ulimi, komanso kukhazikitsa magulu ndi mabungwe a mphamvu woyimira zofuna zawo.
- (vi) Kuteteza nzeru, luso, luntha ndi njira zomwe makolo akhala akugwiritsa ntchito posamalira ndi kusunga mbewu: Alimi ali ndi ufulu woteteza njira za makolo zomwe zili pachiopsezo choyiwalika kapena kusiyidwa kugwiritsidwa ntchito.
- (vii) Kudyerera phindu lopezeka kudzera mu mbewu ndi njira zomwe makolo awo akhala akugwiritsa ntchito kwa nthawi yayitali: Ufulu uwu ndiwovomerezeka ndi ndondomeko za bungwe lalikulu pa dziko lonse la United Nations (UN).

Maiko onse adavomera kuti mbewu zakhala zikutetezedwa, kusamalidwa ndi kusungidwa kwa zaka zambiri ndi alimi a m'madera, komanso m'maiko omwe zidachokera. Mbewu zakhala zikusintha mogwirizana ndi zosowa za anthu, kusintha kwa nyengo, komanso kuti zithandize mokwanira pothetsa njala.

Nthambi ya United Nations (UN) yoona za chakudya pa dziko lonse ya Food and Agriculture Organisation (FAO) idavomereza za ufulu wa alimi m'zaka za m'ma 1980. M'chaka cha 2001 mgwirizano woona za mbewu zomwe zimaperaka chakudya pa ulimi ndi chakudya pa dziko lonse la International Treaty on Plant Genetic Resources for Food and Agriculture udavomerezanso kuti alimi ali ndi ufulu wawowawo wa padera. M'chaka cha 2002, Malawi ndi maiko ena adasayina komanso kulonjeza kuti adzakwaniritsa mfundo za mgwirizanowu. Choncho dziko la Malawi ndilokakamizika kukwaniritsa ndondomeko zonse za mgwirizanowu. Mukafuna kudziwa zambiri za mgwirizanowu mutha kuzipeza pa mutu wachinayi wa mgwirizanowu. Muthanso kuwerenga zambiri pa makina anu a kompyuta potsegula pa <http://www.planttreaty.org>.



Chionetsero cha mbewu zosiyanasiyana monga chimanga chamakolo, nyemba, maungu, soya, mapira ndi therere kuonetsa kuchuluka kwa chakudya chosiyanasiyana chopezeka kumudzi

Mkulu wina wogwira ntchito yokhudzana ndi ufulu wa anthu ku United Nation (UN), a Olivier de Shutter, m'chaka cha 2013 adati anthu oposa theka a m'dziko la Malawi ndi osauka, komanso theka la ana a m'dzikomu akudwala matenda operewera zakudya m'thupi. Iwo adati ngakhale anthu ndi maiko ambiri amatenga dziko la Malawi ngati la chitsanzo pa nkhani yochepetsa njala pogwiritsa ntchito zipangizo za ulimi zotsika mtengo (Farm Input Subsidy Programme) zomwe boma limagulitsa, Malawi ikulephera kupatsa alimi mphamvu zoti azidzidalira ndi kudziyimira paokha.

Lipoti la m'chaka cha 2014 lofotokoza momwe maiko akuvutikira ndi njala, likuwonetsa kuti kuyambira m'chaka cha 2005 njala yakhala ikuchepa m'dziko la Malawi. Malawi ndi limodzi mwa maiko omwe adakwanitsa mfundo ya United Nations (Millennium Development Goal) yochepetsa njala ndi theka pofika m'chaka cha 2015 ngakhale anthu ena m'dziko muno akusowabe chakudya.



Munda ochulukitsilapo mbewu ya mawere pa Chikwawa Community Seed Bank

ZOMERA ZOSIYANASIYANA ZA M'DZIKO LA MALAWI

Dziko la Malawi ili ndi zomera zosiyanasiyana zomwe zimapezekanso m'madera osiyanasiyana. M'dziko muno muli mitundu pafupifupi 555 ya zomera zodyedwa ndi zosadyedwa zomwe. Zina mwa mbewu zodyedwazo ndi chimanga, mpunga, mapira, chinangwa, mbatatata, nyemba ndi nthochi.

Malawi ilinso ndi mitundu yosiyanasiyana ya chimanga. China ndi chamakolo ndipo chimawoneka mosiyanasiyana-chakuda, choyera, chofira, chachikasu-pamene china chilinso ndi mitundu, komanso maso osiyanasiyana.

Malawi ilinso ndi mitundu yosiyanasiyana ya mpunga yomwe imadziwikanso ndi maina osiyanasiyana. Mpunga wa m'dziko muno uli ndi kuthekera kosiyanasiyana kolimbana ndi matenda, tizilombo towononga mbewu, komanso ndiwopilira ku chilala. Akatswiri opanga ndi kuchulukitsa mbewu, komanso mibado ili n'kudza idzatha kuwudalira mpungawu pogonjetsa njala.

KODI UFULU WA ALIMI UNGAKWANIRITSIDWE BWANJI?

Alimi ali ndi ufulu wopitiriza kuchita zomwe akhala akuchita mu zaka zambiri zomwe zapitazo: monga kusunga mbewu za makolo ndi kuzipititsa patsogolo makamaka panopa pamene nyengo ndi zofuna za anthu zikusintha.

M'chaka cha 2010 bungwe la United Nations (UN) loona za chakudya ndi ulimi pa dziko lonse la Food and Agriculture Organisation (FAO) mu lipoti lake la za mbewu lidasindikira kufunika kotu alimi azisunga ndi kuteteza mbewu za makolo m'minda mwawo kuphatikizirapo zoyiwalika kapena zomwe zili pachipsyezo choti zikhoza kutha.



Alimi Chrissy Mazengera ndi Letina Nemiya ochokera ku Dowa, Mvera kuonetsa mbewu zawo zosiyanasiyana za chimanga chamakolo, nyemba, mfutso, mchewere, malambe ndi zina zomwe amasunga ndikudya kumudzi. Uku kunali ku chionetsero cha mbewu ndichakudya ku Mzimba.

Mbewu za makolo ndi mbewu zomwe alimi akhala akulima kwa zaka zambiri ndipo zidazolowera kapena zimachita bwino m'madera omwe zimalimidwa. Mbewu za makolo ndi zopilira ku matenda, tizilombo towononga mbewu, komanso ku nyengo zosiyanasiyana za m'madera omwe zakhala zikulimidwa.

Mbewu za makolo ndi zina zomwe alimi sakonda kubzala ndi zofunika kaamba kotu zimathandiza alimi kupeza zosowa zawo, komanso kupherera kusintha kwa nyengo. Mbewuzi ndi zomwe alimi ang'onoang'ono amadalira ndipo zimathandiza akatswiri omwe amapanga mbewu kudziwa zofuna za anthu, komanso kupeza mbewu yopilira mokwanira

ku chilala poganzira nyengo ya m'deralo. N'zofunika kukumbukira kuti mbewu zonse za makono zomwe akugwiritsa ntchito panozi zidachokera ku zomera zosiyanasiyana.

Mbewu za makolo ndi mbewu zomwe zidazolowera nyengo ya m'madera momwe zakhala zikubzalidwa. Mbewuzi zimachita bwino m'maderawo, komanso zimapatsa thanzi. Mbewuzi zili ndi ntchito zosiyanasiyana, kuwonjezera apo n'zopilira ku matenda komanso tizilombo towononga mbewu. Ngakhale mbewu za makolo n'zothandiza, zambiri zikusowa ndipo zina mwa zifukwa zomwe zikuchititsa ndi izi:

- Mbewu za makono zalowa m'malo mwa za makolo ndipo izi zikuchititsa kuti mbewu zambiri za makolo zisamabzalidwense. Ngati mbewu siikubzalidwa, pakhalekhale imasowa kapena kuti imatha osapezekanso;
- Kusintha kwa nyengo komwe kumachititsa mbewu zambiri kuti zizigwidwa ndi matenda, komanso tizilombo tachilendo;
- Kusowa kwa ulangizi, malamulo, ndalama ndi dongosolo lothandiza kupititsa patsogolo mbewu zatsopano kuchokera ku mbewu zomwe alimi adazolowera kuzilima.

Umodzi mwa mgwirizano wofunika kwambiri wa maiko wa m'chaka cha 1992 wolimbikitsa kusamalira ndi kugwiritsa ntchito mosamala zachilengedwe wa Convention on Biological Diversity (CBD) udamanga mfundo zothandiza kupititsa patsogolo mitundu yosiyanasiyana ya mbewu, ziweto ndi zachilengedwe zina zambiri. Mwa zina, maiko adagwirizana kuti pofika m'chaka cha 2020 adzakhale atateteza magawo 70 mwa magawo 100 aliwonse a mitundu ya mbewu, zomera za kutchire, komanso kuteteza njira zomwe makolo akhala akutsata polima ndi kusamalira mbewu ndi zomerazo.

NJIRA ZOTETEZERA MBEWU NDI ZOMERA ZAM'NTCHIRE

Pali njira zosiyanasiyana zotetezera mbewu za makolo ndi zomera zam'ntchire. Zina mwa njirazo ndi izi:

- Kusunga mbewu ndi zomera m'malo osungira mbewu a kumudzi ndi m'minda yomwe zachilengedwe

zochokera m'maiko osiyanasiyana zimasungidwa, komanso kutetezedwa. Alimi ang'onoang'ono alinso ndi njira zawo zosungira mbewu monga kuziika m'mbiya, m'zikwatu, maenje ndi m'mabanki a mbewu a m'midzi. Ndibwino kulimbikitsa alimi kusunga mbewu m'malo osungira mbewu akuluakulu. Mbewu ndi zomera zimatengedwanso kuchokera ku malo womwe zidazolowera ndi kupita nazo ku malo osungira mbewu akuluakulu a m'maiko akunja;

- Kusunga ndi kuteteza za chilengedwe m'malo momwe zidazoloweramo;
- Kusunga ndi kuteteza mitundu yosiyanasiyana ya mbewu za makolo ndi za chilengedwe zina m'minda. Alimi ang'onoang'ono akhala akuchita izi kwa zaka zambiri. Chaka chilichonse alimi amasunga mbewu zoti adzabzale chaka chotsatiracho. Amalimanso mbewu zosiyanasiyana m'minda yawo ing'onoing'ono ya pa khomo kuti apeze chakudya chokwanira pa banja pawo, komanso ateteze mbewu za makolo.

10

Malingana ndi kafukufuku yemwe adachitika m'chaka cha 2008 wofotokozza za mbewu ndi chakudya m'dziko muno, palibe njira zenizeni zomwe zingathe kugwiritsidwa ntchito mokwanira poteteza ndi kusunga mbewu m'minda. Ichi n'chifukwa chake ntchito zambiri zosunga mbewu m'minda zimangothera pa kafukufuku.

NJIRA ZOLIMBIKITSIRA UFULU WA ALIMU, KOMANSO NTCHITO YOSUNGA NDI KUTETEZA MBEWU M'MINDA YAWO

A. Malo osungira mbewu kumudzi

Malo osungira mbewu kumudzi amaluzanitsa ntchito yochulukitsa, kusunga, kusinthanitsa, kugulitsa ndi kusankha mbewu zosiyanasiyana zomwe alimi ang'onoang'ono amalima ndi kusamalira m'magulu ndi cholinga choti asamavutike kuzipeza akazifuna. Kudzera m'malo osungira mbewu kumudzi, alimi amasonkhanitsa ndi kusunga mbewu zawo m'magulu. Malowa amathandiza kuti alimi asamavutike kupeza mbewu mu dzinja ndipo amalimbikitsa ufulu wawo wosunga, kusinthanitsa, kugwiritsa ntchito ndi kugulitsa mbewu m'magulu. Zina mwa ntchito za malo

osungira mbewu kumudzi ndi izi:

- Kuthandiza alimi kupeza mosavuta mbewu zomwe zimachita bwino m'madera mwawo;
- Kusunga mbewu ndi kugwiritsa ntchito moyenera zachilengedwe;
- Kulimbikitsa ntchito yochulukitsa, kusunga, kuteteza, kusinthanitsa ndi kugulitsa mbewu za makolo pakati pa alimi ang'onoang'ono;
- Kuthandiza alimi kupeza mosavuta mbewu zamakolo pa nthawi ya ngozi zogwa mwadzidzidzi, komanso kuzisunga kuti zisayiwalike kapena kutha.

Mgwirizano wa pa dziko lonse woona za mbewu zomwe zimapereka chakudya pa ulimi wa International Treaty on Plant Genetic Resources for Food and Agriculture ukutsimikiza kuti mabanki a mbewu akumudzi amathandiza posamalira za chilengedwe, kuteteza nzeru za makolo, kulimbikitsa alimi kutenga nawo gawo yopanga ziganizo pa nkhani za ulimi, komanso kuwapatsa mphamvu zosamalira ndi kupanga nawo mbewu zomwe zingachite bwino m'dera lawo.



Chikwatu chosungila ndiwo zamasamba

Malo osungira mbewu kumudzi amapatsa alimi mwayi wozeza phindu lokwanira kuchokera ku mabungwe ndi makampani omwe amagwiritsa ntchito mbewu ndi nzeru zawo pa malonda. Izi zimathandizanso kuluzanitsa alimi ndi malo osungira mbewu

kumudzi ndi malo akuluakulu osungirako zachilengedwe zochokera maiko osiyanasiyana, komanso mgwirizano waukulu wa za ulimi wa International Treaty on Plant Genetic Resource for Food and Agriculture.



Kasungidwe ka dowe ndi khobwe zomwe amamangilila kudenga kwa malo ophikira.



Lead Farmer wa FYF, Etrida Luhanga, wa ku Chikwawa ku Rumphu kuwonetsa mmene amakusungila chimanga.

Malo osungira mbewu a kumudzi amaperekanso mwayi kwa alimi ochokera m'madera osiyanasiyana kukumana ndi

kusinthana mbewu ndi zomera zina zomwe zimakabzalidwa m'madera achilendo ndi cholinga cholimbikitsa maderawo kupititsa patsogolo mbewu, komanso ntchito zothetsa njala ndi chitukuko cha m'maderawo.

Alimi eni ake ndiwo amayendetsa ntchito za malo osungira mbewuwa mothandizidwa ndi atsogoleri omwe amasankha. Ena mwa maphunziro womwe anthu oyendetsa malo osungira mbewu a kumudzi amalandira ndi awa:

- Kusunga m'ndandanda wa mitundu ya mbewu, kuchuluka kwake ndi zina;
- Kukonza dongosolo la magawanidwe a mbewu (potengera ndi kalemba wa ngongole zomwe alimi adatenga, komanso kubweza), kalondolondo wawo, komanso mmene ntchito yochulukitsa mbewu yayendera;
- Kutsata ndondomeko zothandiza kusunga mbewu mwadongosolo kuti zisawonongeke;
- Luso lodziwira kuchuluka kwa chinyontho chomwe chili mu mbewu;
- Njira zosiyanasiyana zosungira mbewu (monga m'matumba, mbiya, muzikwatu, nkhekwe ndi zina);
- Kudziwa anthu, mabungwe ndi makampani omwe amagulitsa mbewu m'deralo;
- Dongosolo loyendetsera ndalama ndi gulu (malamulo woyenera gulu kuwatsata pa kasungidwe ndi kagwiritsidwe ka chuma chake).

Malingana ndi katswiri wodziwika bwino pa nkhani zosunga mbewu, a Ronnie Vernoo, malo osungira mbewu a kumudzi akuthandiza kwambiri popanga ndi kuchulukitsa mbewu zomwe makampani, mabungwe, madipatimenti ndi maunduna aboma amagula.

Ntchito zina zikuluzikulu zomwe malo osungira mbewu kumudzi amagwira ndi izi:

- Kupereka ngongole ya mbewu kwa mamembala ake mudzinja;
- Kuwonetsa kuti mamembala ake onse omwe adakongola mbewu abweza;
- Kusamalira mbewu kuti zisawonongeke;
- Kuteteza mbewu ku anankafumbwe,

makoswe ndi zilombo zina zowononga mbewu;

- Kutenga nawo mbali pa ntchito yochulukitsa mbewu, kuchita nawo kafukufuku wa mbewu, kuyang'anira makomiti ndi mamembala ake.

M'dziko la Malawi muli malo osungira mbewu ambiri omwe ali m'madera a za ulimi a m'boma la Rumphu a Bolero, Mhuju ndi Katoma. Mwa malowa ndi ochepa omwe akugwirabe ntchito. Ambiri mwa malowa adamangidwa m'chaka cha 2010 ndi bungwe la Find Your Feet (FYF) ndi thandizo lochokera ku bungwe la Development Fund of Norway, komanso la European Union (EU).

ZOKAMBIRANA

1. Chitani kalondolondo ndi kukambirana ndondomeko za mbewu za dziko la Malawi.
2. Tchulani malo osungirako mbewu a kumudzi womwe mumawadziwa ndipo fotokozani mwatsatanetsatane njira zomwe zimagwiritsidwa ntchito pokwaniritsa ufulu wa alimi wokwatitsa, kupanga, kuteteza ndi kusinthanitsa mbewu.
3. Kambiranani kufunika kwa malo osungira mbewu a kumudzi pa ntchito yothetsa njala. Pezani njira zomwe zingathandize powapititsa patsogolo;
4. Fotokozani kufunika kokhazikitsa malo osungira mbewu owonjezera. Tchulani mbewu zomwe zili zofunika kwambiri kuzisunga, kuzichulukitsa ndi kuzigawa.

B. Kutenga nawo gawo posankha mitundu ya mbewu

Ngakhale fetereza amathandiza kuti mbewu zichite bwino, kusamalira bwino mbewu, kuziteteza ku matenda, zilombo ndi kugula mbewu zabwino zamakono kumathandizanso mlimi kuti akolole zochulukuka. Mbewu zabwino, komanso zobereka kwambiri ndi chida champhamvu chothetsera njala m'dziko.

Nthawi zambiri alimi amadalira akatswiri a zasayansi ndi makampani osiyanasiyana kuti awakwatitsire kapena kuwapangira mbewu yatsopano. Cholinga chopangira kapena chokwatitsira mbewu ndi kuyipanga kuti izibereka zochulukuka, ikhale yopilira ku chilala,

matenda, zilombo zowononga mbewu, yocha msanga, yoyenda malonda, komanso yosavuta pokolola.



Lead Farmer wa FYF, Juliana Ngwira, Kuwonetsa mmene amasamalira mbewu yachimanga mmunda.



Mai Sarah Mkandawire ochokera mmudzi mwa Group Village Headman Bulawula, mmodzi wa alimi a BCI membala wa nyumba yokusungilamo mbewu ya Mkombezi, amene amachulukitsa mbewu ya mtedza.

Masiku ano sayansi yapita patsogolo, akatswiri amatha kutenga chikhalidwe cha zomera za kutchire ndi kuchika mu mbewu zomwe alimi amalima kuti zizichita bwino pobereka, komanso zizipilira ku matenda ndi chilala.

Ganizo lolimbikitsa alimi kutenga nawo gawo posinthanitsa ndi kuchulukitsa mbewu lidadza malingana ndi kafufukuku yemwe adachitika m'zaka za m'ma 1980. Kuchokera nthawi imeneyo, alimi akhala akutenga nawo gawo popititsa patsogolo mbewu za mitundu yosiyanasiyana. Bungwe lalikulu la pa dziko

lonse la United Nations (UN) ndi mabungwe ena omwe amathandiza maiko pa zitukuko zosiyanasiyana adatsimikiza za kufunika koti alimi azitenga nawo gawo pa kafufukufuku, komanso pochulukitsa mbewu ndi nzeru zasayansi.



Alimi kugwiritsa ntchito 4-Cell Analysis posankha mitundu yambewu zomwe zikupezeka ndi kulimidwa ku Baliro, Katowo Extension Planning Area.

Kafukufuku yemwe alimi amatenga nawo gawo pa zochitikachitika ndi wabwino pa zifukwa ziwiri: amakhala wosabowola m'thumba, komanso alimi ndi mabungwe amapeza luso ndi nzeru zina zopititsira patsogolo ulimi.

Akatswiri a zasayansi amakhulupirira kuti ntchito zosiyanasiyana ziyende bwino, alimi ndi mabungwe ayenera kutenga nawo gawo. Alimi, mafumu ndi atsogoleri ena akatenga nawo gawo amadziperereka ku ntchito za chitukuko, kuthandiza kupititsa patsogolo ndondomeko, malamulo ndi njira za makono zomwe zikufalitsidwa. Kulimbikitsa alimi kutenga nawo gawo kumapinduliranso mabungwewo popeza amatha kugwiritsa nawo ntchito mosavuta nzeru za makolo zomwe alimi a m'deralo akhala akugwiritsa ntchito kwa zaka zambiri. Izi zikutanthauza kuti sayansi imapindula kwambiri pogwiritsa ntchito nzeru za makolo mosavuta. Choncho mabungwe angafikire alimi ambiri pogwiritsa ntchito njirayi, koma pochita izi azindikire ndi kuvomereza ntchito yotamandika yomwe alimi achizimayi amagwira. Choncho pasamakhale kusiyana pakati pa abambo ndi amayi.

C. Kutenga nawo gawo popanga mbewu

Kutenga nawo gawo popanga mbewu kumakhudza alimi, akatswiri asayansi, alangizi, ogulitsa mbewu ndi mabungwe omwe

akugwira nawo ntchito yopanga mitundu yosiyanasiyana ya mbewu, kuyichulukitsa ndi kuyigawa.

Posiyantsa ndi kuchulukitsa mbewu wamba komwe akatswiri a zasayansi amapanga ziganizo zonse okha, apa ndi pamene, alimi amamanga nawo mfundo (kukhazikitsa nawo zolinga), kusankha ndi kupereka makolo a mbewu zoti zichulukitsidwe, kupereka malo ogwirira ntchitoyo, kukambirana zotsatira ndi akatswiri a zasayansi, kukhazikitsa ndondomeko za zochita chaka chotsatira, kupereka maganizo a zinthu zoyenera kuzisintha, kuchita nawo kalondolondo wa mitundu ya mbewu, komanso kugulitsa nawo mbewuyo. Alimi achizimayi ndi wofunika kwambiri pa ntchitoyi kaamba koti amakhala ndi luntha lozama pa nkhani zaulimi. Alimi achizimayi amakhalanso ndi zofuna, komanso chidwi chapadera pa nkhani yothetsa njala kaamba koti ndiwo amasamalira mabanja ndi anthu pamudzi.

Kupereka mwayi kuti aliyense atenge nawo gawo kumathandiza kuti alimi, azasayansi, alangizi ndi mabungwe agawane luso lawo pa nkhani yopanga mbewu zatsopano zogwirizana ndi zofuna za alimi, komanso ogula.

Izi ndi zina zomwe ziyenera kutsatidwa popanga mbewu:

- Kuvomereza kufunika kwa mbewu ndi nzeru za makolo;
- Kupeza njira zogwiritsira ntchito mbewu za makolo posintha mitundu ya mbewu kuti yigwirizane ndi zofuna za alimi;
- Anthu omwe amagwiritsa ntchito kapena kupindula ndi mbewuzo amatenga gawo lalikulu lofotokoza zofuna zawo;
- Anthu omwe amagwiritsa ntchito kapena kupindula ndi mbewuzo amatenga gawo lalikulu pomanga mfundo kapena kupanga ziganizo;
- Anthu omwe amagwiritsa ntchito kapena kupindula ndi mbewuzo amakhala ndi udindo waukulu pa ntchito yopanga mbewu;
- Anthu amakambirana ndi kugwirizana zochita;
- Abambo ndi amayi amapatsidwa mwayi wofanana.

Phindu lotenga nawo gawo popanga mbewu

ndi loti onse; alimi ndi akatswiri a za sayansi omwe, amapeza luso ndi luntha latsopano. Kupatula apo, alimi ndi akatswiri azasayansi sakanizana kapena kukokanokokana pakafunika kuti mbewu ndi luso la makolo ligwiritsidwe ntchito popanga mbewu zatsopano.



Akuluakulu a kunyumba yosungilako mbewu ya dziko la Malawi (Malawi Plant Genetic Resources Centre) kugwira ntchito ndi alimi polimbikitsa kusunga mbewu zosiyanasiyana

ZOKAMBIRANA

14

Fotokozani m'mene kutenga nawo gawo kwa alimi pa ntchito yopanga mbewu kungalimbikitsire ufulu wawo wogwiritsa ntchito ndi kupititsa patsogolo mbewu zatsopano zopilira ku chilala, matenda ndi zilombo zowononga mbewu;

Kambiranani zoyenera kuchita kuti alimi atenge nawo gawo pa ntchito yopanga mbewu. Nanga ubwino wake ndi wotani?

D. Kusamutsa mbewu m'dera kapena m'dziko lina ndi kupita nazo linzake

Monga zakambidwa kale, mabungwe amasunga mbewu m'mabanki akuluakulu. Mbewu zachilendo zomwe zimapezeka m'mabankiwo zimachokera m'minda ya alimi ang'onoang'ono.

Alimi ali ndi ufulu wopititsa mbewu zawo m'madera ena kuti akazisunge ndi kuzisamalira m'minda ya m'maderawo ngati mbewu zachilendo.

Alimi ali ndi ufulu wobwezeretsanso mbewu zomwe zidatengedwa m'madera awo ndi kukazisunga m'minda ya m'madera awo kapena m'maiko ena. Ndongomeko zoyenera kuzitsata pobwezeretsa mbewu sizisiyana ndi zomwe adatenga potumiza mbewuzo m'maikowo. Nthawi zambiri

mbewu zikamadzabwezeretsedwa zimakhala zitayiwalikira m'madera omwe zidachokerawo.



Mbewu ya chimanga cha lokolo.



Mbewu ya mawere ndi zina mwa mbewu zomwe zikusungidwa ku nyumba yosungila mbewu ya dziko la Malawi (National Genebank) ya Chitedze.

Kubwezeretsa mbewu ndi chitsanzo chabwino cha mmene mbewu ya m'dera lina angaisungire m'minda ya m'madera kapena maiko ena ngati mbewu yachilendo.

ZOKAMBIRANA

1. Fotokozani mbewu zoyiwalikira m'madera mwanu. Nanga ndi mbewu ziti zomwe ziyenera kutumizidwa m'maiko ena kuti akazisunge kaamba koti n'zofunika?
2. Fotokozani maiko omwe akusunga mbewu zoyiwalikira za dziko la Malawi. Nanga tingatsate ndondomeko zotani kuti tizibwezeretse m'dziko muno?

Kumbukirani: Alimi ali ndi ufulu woteteza ndi kugwiritsa ntchito mbewu zomwe zasungidwa m'minda mwawo. Alimiwo ayenera kupeza mbewuzo mosavuta kaamba koti ndi

zothandiza pothetsa njala m'madera mwawo. Sibwino kuphwanya ufulu wa alimi wogwiritsa ntchito mmene akufunira mbewu zomwe amasunga m'minda mwawo.

3. Alimi ali ndi ufulu wosinthanitsa kapena kugulitsa mbewu zomwe amasunga m'minda mwawo

Alimi ali ndi ufulu wogulitsa mbewu zomwe akhala akusunga m'minda mwawo kwa zaka zambiri. Alinso ndi ufulu wogulitsa mbewuzo m'misika ya m'dziko mwawo, komanso ya m'maiko akunja ngakhale kuti maiko ambiri amafuna mbewu zovomerezeka zokhazokha. Amafuna mbewu zokhazo zomwe malamulo akuvomereza kuti zigulitsidwe. Mbewu zina zonse zomwe alimi ang'onoang'ono amagulitsa amati n'zosavomerezeka.

Khalidwe la alimi losinthanitsa mbewu lidayamba kalekale. Alimi atha kugulitsa mbewu kwa anzawo, m'misika ikuluikulu ya m'dziko mwawo komanso ya maiko akunja.



Alimi kusinthana mbewu ya chimanga chalokolo.

NJIRA ZOKWANIRITSIRA UFULU WA ALIMI WOSINTHANITSA, KOMANSO KUGULITSA MBEWU ZOCHOKERA M'MINDA MWAUO

A. Chiwonetsero cha mbewu cha kumudzi

Chiwonetsero cha mbewu cha kumudzi ndi imodzi mwa njira zabwino zogawanirana nzeru ndi luntha pakati pa alimi, akatswiri azasayansi, makampani, ogwira ntchito zaboma, komanso atolankhani. Alimi amakhala ndi mwayi owonetsa mbewu zosiyanasiyana za m'madera mwawo. Ziwonetsero za mbewu zimalimbikitsanso ntchito yosinthanitsa mbewu. Ziwonetserozi zimalimbikitsanso ufulu wa alimi wosinthanitsa mbewu zosungidwa m'minda mwawo moti alimi amakhala ndi mwayinso wosunga makolo a mbewu zosiyanasiyana.



Lead Farmer wa Mzuzu ADD a Whitehead Chabvula aku Hora kulongosolera alimi anzawo mmene amasamalira mbewu pa tsiku lachionetsero cha alimi.



Kuwonetsa kasungidwe ka mbewu muzikho patsiku lachionetsero cha mbewu ndi chakudya chomwe chinachitika ku Mbawa mu boma la Mzimba.

Ziwonetsero za mbewu zimalimbikitsa ufulu wa alimi motere:

- Kuthandiza alimi kusinthanitsa mbewu;
- Kulimbikitsa alimi kupeza mbewu zatsopano zopilira ku chilala, matenda ndi zilombo zowononga mbewu;
- Kulimbikitsa ntchito yogawana luso ndi nzeru zomwe makolo akhala akugwiritsa ntchito kwa zaka zambiri;
- Kulimbikitsa kusunga ndi kugwiritsa ntchito mbewu za makolo;
- Kupereka mwayi kwa alimi wokonzza zokolola zawo kuti azipeza phindu lochuluka.

Ziwonetsero za mbewu zimathandiza alimi ang'onoang'ono kulengezetsa kapena kutsatsa mbewu zawo kwa anthu ambiri pakamodzi. Zimawapatsa alimi mwayi wochulukira wosinthanitsa, komanso wogulitsa zokolola zawo mosavuta. Kusinthanitsa mbewu kumabwezeretsa mbewu zoyiwalika m'madera osiyanasiyana, kupatsa mwayi wosintha mbewu za makolo kuti zizibereka kwambiri. Zimawapatsanso alimi mphamvu pa mbewu zawo, komanso kudziwitsa anthu za ufulu wa alimi.

Chiwonetsero cha mbewu cha m'boma la Rumphu

Ziwonetsero za mbewu zimapititsa patsogolo luso la alimi pa kasungidwe ndi kasinthanitsidwe ka mbewu. Alimi amakhalanso ndi mwayi wophunzira luntha la anzawo ochokera m'madera ena makamaka pa kugwiritsidwe ka ntchito ka mbewu ndi zachilengedwe zina. Alimi amagulitsa mbewu zawo, komanso kuwonetsa nzeru zomwe makolo awo akhala akugwiritsa ntchito kwa zaka zambiri. Kwa akatswiri woona ndi kusamalira zachilengedwe, ziwonetsero za mbewu zimawapatsa mwayi wodziwa za zachilengedwe zomwe zimapezeka m'madera osiyanasiyana.

Ndithandizo lochokera ku Development Fund of Norway, bungwe la Biodiversity Conservation Institute (BCI) mogwirizana ndi Centre for Environmental Policy and Advocacy (CEPA), Find Your Feet (FYF), komanso Mzuzu Agriculture Development Division (MZADD) adakonza chiwonetsero cha mbewu pa banki ya mbewu ya Chikwawa ya m'boma la Rumphu. Mutu wa chiwonetserocho udali Kuchulukitsa Zokolola ndi Kuthetsa Njala pa Banja Pamene Kusintha kwa Zanyengo Kwafika Povuta.

Mlendo wolemekezeka pa chiwonetserocho adali wapampando wa komiti yoona za ulimi ya ku Nyumba ya Malamulo, a Felix Jumbe, amenenso ali phungu wa m'dera la pakati m'boma la Salima.

Chiwonetserocho chidapatsa mwayi bungwe la Centre for Environmental Policy and Advocacy (CEPA), Development Fund of Norway ndi Global Forum on Agriculture Research wokambirana ndi atsogoleri osiyanasiyana kuphatikizirapo wapampando wa komiti yoona za ulimi m'Nyumba ya Malamulo kufunika kolimbikitsa ufulu wa alimi.

ZOKAMBIRANA

1. Fotokozani mmene ziwonetsero za mbewu zimene mudachitapo zidalimbikitsira ntchito yopititsa patsogolo, kusamalira ndi kugwiritsa ntchito moyenera mitundu yosiyanasiyana ya mbewu, kuteteza nzeru za makolo, ufulu wa alimi wosinthanitsa, komanso kugulitsa mbewu zosiyanasiyana.
2. Fotokozani njira zomwe zingagwiritsidwe ntchito pa ziwonetsero za mbewu pofuna kuteteza mbewu zofunika kwambiri, komanso zomwe zili pa chiopsezo choyiwalika.
3. Kambiranani njira zolimbikitsira, komanso kupititsa patsogolo ufulu wa alimi wosungu, kuteteza, kusinthanitsa ndi kugulitsa mbewu zomwe amasungu m'minda mwawo.

Mafunso otsogolera pa ntchitoyi:

- Kodi ndi mbewu yochulukira bwanji yomwe idasinthanitsidwa pa chiwonetsero chomwe inu mudachita nawo?
- Nanga ndi anthu ochulukira bwanji omwe adachita nawo? Amayi adalipo angati? Kodi ntchito za abambo ndi amayi pa chiwonetserocho zidali zotani?
- Ndi mitundu iti ya mbewu yomwe idasinthanitsidwa mochulukira? Nanga chikhaliidwe chake chidali chotani?
- Nanga ndi nzeru zotani za makolo zomwe alimi adasinthana?

B. Kupeza misika

N'zoona alimi ali ndi ufulu wogulitsa mbewu zomwe amasungu m'munda mwawo, koma kuti ufuluwu utheke ayenera kupeza misika m'dziko mwawo komanso m'maiko akunja.

Njira imodzi yokwaniritsira ufulu wa alimi wogulitsa mbewu za m'munda yawo ndi kupeza njira zodalirika zotsatsira mbewuzo. Pafunika kusanthula ndi kufotokoza m'omveka ubwino weniweni wa mbewuzo ndi cholinga chopereka chikhumbokhumbo mwa ogula.

Njira ina ndi kukonza mbewu (kuwonetsetsa kuti mbewu zomwe alimi akolola zikuwoneka bwino, zalongedzedwa bwino mu mapakete olembedwa bwino, komanso momveka). Kukonza mbewu kumachititsa kuti anthu agule zinthu za makono, zowoneka bwino, komanso zosavuta kugwiritsa ntchito. Kulumikizana kwa

mlimi ndi wogula ndi kofunika kwambiri pa malonda.

Zokambirana za ufulu wa alimi wogulitsa mbewu zawo, sizingathe osaunikiranapo za malamulo okhudza malonda a mbewu. Malamulo a maiko ambiri amati mbewu iyenera kuvomerezedwa isadaikidwe pa msika. Choncho alimi ambiri ang'onoang'ono amavutika kuti agulitse mbewu zawo kaamba koti ambiri sakhala ndi chilolezo. Apa maiko ayenera kukhazikitsa malamulo ndi cholinga cholimbikitsa ufulu wa alimi wogulitsa ndi kusinthanitsa mbewu zawo. Izi zitha kupititsa patsogolo, komanso kukwaniritsa ufulu wawo wochita malonda.

Malamulo ololeza alimi kugulitsa ndi kusinthanitsa mbewu zawo sayenera kuphwaya ufulu wawo wogulitsa mbewu zawo. M'malo mwake boma ndi alimi agwirizane mmene malonda a mbewu angamayendere.

Malamulo omwe dziko la Malawi likugwiritsa ntchito padakali pano sakupatsa mwayi alimi ang'onoang'ono ogulitsa mbewu zawo.

ZOKAMBIRANA

Kambiranani kukula kwa msika wa mbewu za makolo womwe uli m'dziko la Malawi ndi njira zothandiza kulimbikitsira malonda a mbewuzo. N'chiyani choyenera kuchita pofuna kupititsa patsogolo malonda a mbewu?

Kumbukirani: Alimi ali ndi ufulu wogulitsa, komanso kusinthanitsa mbewu zawo. Ziwonetsero za mbewu n'zothandiza kaamba koti zimalimbikitsa alimi kusinthanitsa mbewu zawo. Alimi ali ndi ufulu wogulitsa mbewu zawo m'dziko mwawo, komanso m'maiko akunja. Maiko ayenera kukhazikitsa malamulo ndi ndondomeko zothandiza alimi kukwaniritsa ufulu wawo wogulitsa, komanso kusinthanitsa mbewu zomwe amalima. N'kofunikanso kukhazikitsa malamulo wolimbikitsa alimi kugulitsa mbewu za makolo.

4. Ufulu wa alimi wotenga nawo gawo pomanga mfundo za m'dziko lawo zokhudza mbewu ndi ulimi

Ufulu wa alimi sungakwaniritsidwe pokhapokha atawapatsa mwayi wotenga nawo gawo lokambirana malamulo, ndondomeko zoyendetsera ulimi, masungidwe ndi magwiritsidwe ntchito oyenera a mbewu.

Pokhapokha alimi atakhala ndi chidziwitso chokwanira ndi kutsatira bwino nkhani zomwe zikukambidwa, sangatenge nawo gawo lokwanira pa zokambirana. Choncho alimi ayenera chidziwitso chokwanira zokambirana zisadayambike kuti athe kutenga nawo gawo lokwanira pa zokambiranazo.



Pamwamba ndi pansi: Alimi kupereka mfundo zawo pa misonkhano yozokambilana za mbewu.



N'zofunika kuzindikira kufunika koti alimi azitenga nawo gawo pa zokambirana makamaka zomwe zikukhudza ntchito yosunga ndi kuteteza mbewu ndi nzeru za makolo. Alimi amange nawo mfundo zokhudza kupanga malamulo ndi ndondomeko zatsopano za ulimi, komanso kuchita nawo kalondolondo wa za ulimi.

Alimi amatenga nawo gawo mokwanira akakhala:

- Omasuka, komanso akapatsidwa mwayi wolankhula;
- Ndichidziwitso chokwanira cha nkhani zomwe zikukambidwazo.

Izi zikutanthauza kuti alimi ayenera kulandira mauthenga, kukhala ndi mfundo, komanso chidziwitso chokwanira chowathandiza kupanga zisankho. Alimi ayenera kuganiza mozama zotsatira za zisankho zomwe apanga

pa ufulu wawo wogulitsa, kusinthanitsa ndi kuteteza mbewu ndi nzeru za makolo.

Nthawi zambiri alimi amangouzidwa mfundo zomwe msonkhano ukuyenera kumanga, koma osapatsidwa mwayi wofotokoza maganizo awo. Ufulu wa alimi wotenga nawo gawo pa zochitikachitika ukuposera pamenepe, ukukhudzanso maubale omwe amapanga, komanso kukonza maphunziro m'madera momwe amachokera ndi cholinga chopititsa patsogolo ufulu wawo.

Ndibwino alimi kutenga nawo gawo pa zokambirana popeza mfundo zomwe amatulutsa zimakhala zopititsa patsogolo ulimi ndi ufulu wawo.

NJIRA ZOTHANDIZA KUKWANIRITSA UFULU WA ALIMI WOTENGA NAWO GAWO PA ZOKAMBIRANA MAKAMAKA PA NKHANI YOSUNGA NDI KUGWIRITSA NTCHITO MOYENERA MBEWU.

A. Alimi omwe amayimirira anzawo m'mabungwe ndi m'magulu omwe amamanga mfundo za ulimi

18

Ufulu wa alimi wotenga nawo gawo pa zokambirana utha kukwaniritsidwa mosavuta alimiwo atapatsidwa mwayi wokhala nawo m'misonkhano ndi m'magulu omwe amakambirana ndi kumanga mfundo kapena kupanga malamulo a dziko okhudza ulimi.

Alimi ang'onoang'ono atha kukhala nawo gawo la zokambirana za dziko kapena maiko kudzera mabungwe ndi magulu awo.

Padakali pano dziko la Malawi likukonza lamulo lokhudza mbewu ndi ndondomeko zoyendetsera mbewuzo. Nthumwi imodzi ya bungwe la Malawi National Seed Board lomwe likukambirana nkhanayi iyenera kukhala mlimi kuti ikayimirire zofuna za anzake pa zokambiranazo.

ZOKAMBIRANA

1. Kambiranani gawo lomwe alimi ang'onoang'ono akhala akutenga pa zokambirani zokhudza ndondomeko ndi malamulo oyendetsera ulimi ndi cholinga chosunga, kuteteza ndi kugwiritsa ntchito mbewu moyenera.
2. Fotokozani zomwe zingawalepheretsa alimi kutenga nawo gawo pa

zokambiranazo. Mwa zina, lingalirani mavuto omwe alimi amakumana nawo kuti apeze mauthenga osiyanasiyana ndi chidwi cha anthu, mabungwe ndi boma chofuna kupititsa patsogolo zofuna za alimi.

B. Kutenga nawo gawo popanga mbewu

Monga tafotokoza kale, kugwiritsa ntchito alimi popanga mbewu zimawapatsa mwayi wotenga nawo gawo pa ntchito yokonza ndi kupanga mbewu zatsopano zomwe zikugwirizana ndi zofuna zawo.

Alimi amakhala ndi mwayi wounika nawo, komanso kukambirana zolinga zazikulu za mbewuzo. Amakhalanso ndi mwayi wosankha mitundu ya mbewu yomwe akufuna kuyipanga, wopha nawo makwacha kudzera mu kugulitsa mbewuzo, komanso kuchita nawo kalondolondo wa mmene ntchitoyo yayendera. Alimi amatenga nawo gawo ndi udindo waukulu wopanga mbewu zatsopanozo.

ZOKAMBIRANA

Fotokozani njira zomwe zingalimbikitse ufulu wa alimi kudzera mu kutenga nawo gawo pa ntchito yochulukitsa mbewu.

Kumbukirani

Alimi ali ndi ufulu wotenga nawo gawo pomanga mfundo zokhudza kusunga, kuteteza ndi kugwiritsa ntchito mbewu zawo. Kutenga nawo gawo pa zokambirana n'kwabwino kuposa kungouzidwa mfundo zomwe ena agwirizana kapena amanga kale. Alimi amatenga nawo gawo loyenera pa zokambirana akakhala ndi chidziwitso chokhudza nkhanu zomwe zikukambidwa, komanso kukhala nako kuthekera kotu athe kuyimirira zofuna za anzawo. Alimi ayenera kukonzekera bwino, komanso kukhala nako kuthekera kotu atha kutsitsa mfundo pa zokambiranazo.

4. Ufulu wa alimi woteteza nzeru, luso ndi njira za makolo zothandiza kusunga ndi kugwiritsa ntchito mbewu moyenera

Kwa nzika ndi alimi ang'onoang'ono, nzeru ndi zikhalidwe za makolo zimakhala gawo la moyo wawo. Nzeru za makolo ndi njira zochitira zinthu zomwe makolo amagwiritsa ntchito kwa zaka zambiri ndipo amaphunzitsa ana ndi zidzukululu zawo osati kudzera mu zolembedwa, koma zongofotokozedwa pakamwa.

Ichi n'cholowa chomwe makolo amachipereka kwa ana awo ndipo chiyenera kutetezedwa popeza ndi gawo la chikhalidwe ndi moyo wawo.

NJIRA ZABWINO ZOKHAZIKITSIRA UFULU WA ALIMI WOTETEZA NZERU, LUNTHA NDI NJIRA ZA MAKOLO ZOSUNGIRA NDI KUGWIRITSIRA NTCHITO MBEWU MOYENERA.

A. Kulemba nzeru ndi njira zomwe makolo akhala akugwiritsa ntchito

Nzeru, luso ndi njira zomwe makolo akhala akugwiritsa ntchito pa ulimi zikuyiwalika pang'onopang'ono kaamba koti achinyamata ambiri sadawaphunzitse. Kuphatikizira apo, achinyamata ambiri alibe chidwi chokhala m'madera akumudzi. Ambiri akumapita m'matauni kukafuna ntchito. Achinyamata ambiri alibe chidwi ndi zikhalidwe za makolo, komanso kuphunzira njira zomwe amatsata potetezera za chilengedwe. Nzeru ndi njira zambiri zochitira zinthu za makolo zikuyiwalika kaamba koti sizidalembedwe m'mabuku. Makolo akafuna kuphunzitsa ana awo amangowafotokozerana. Izi zimachititsa kuti zinthu zina ziywalike.

Njira yokhaya yodalirika yomwe ingathandize kuteteza nzeru za makolo ndi kulemba kuti mibadwo ya mtsogolo idzapindule nazo. Njira ina yokwaniritsira izi ndi kukhala ndi mabuku ofotokoza mndandanda wa zachilengedwe zopezeka m'midzi.

Mabuku a mndandanda wa zachilengedwe ofokokoza mbewu, nzeru, luso ndi njira zapadera zomwe makolo amagwiritsa ntchito m'midzi:

Mabukuwo awonetse mitundu yosiyanasiyana ya mbewu, nzeru, luso ndi njira zomwe makolo akhala akugwiritsa ntchito posamalira zachilengedwe.

Mwa zina, mabukuwo awonetse izi:

- Alimi omwe akusunga mbewu;
- Mayina a mitundu ya mbewu zomwe akusunga;
- Nzeru ndi njira zomwe makolo akhala akugwiritsa ntchito posamalira mbewuzo;
- Zipangizo zosungira mbewu;
- Njira zofetsera kapena kuchulukitsira mbewu;
- Kufotokoza mwatsatanetsatane ngati

mbewuzo zimapezeka mosavuta, movuta kapena zimasowa;

- Zithunzi za mbewu zopezeka m'deramo.



Miimi kufotokoza mmene amapangira nthimphwa, chakudya chopatsa mphamvu ku Hewe mu boma la Rumphu.



Msonkhano olemba nzeru ndi njira makolo amagwiritsa ntchito pa mbewu, zakudya ndi mankhwala ku Chivala EPA mu boma la Dowa.



Fwasani Binwel Mbeya Lead Farmer waku Enyezini, Mzuzu ADD anapeza njira yopangila manyowa a Mbeya.



Andrew Chigoma, Lead Farmer ku Mbalachanda, Mzuzu ADD anapeza njira yopangira manyowa Chinkhuzi.

20

Alimi afotokoze mwatchutchutthu mu mndandandawo mbewu zawo zonse powopetsa kuti ena mtsogolo angadzamati ndi zawo. Izi zimathandiza pokhazikitsa malamulo woteteza mbewuzo ndi kuwonetsetsa kuti azidyera phindu lonse lopezeka mu luso, komanso mbewuzo.

Luso, luntha ndi mbewu zonse za makolo zikalembedwa kumakhala kosavuta kudziwa mwini wake, komanso anthu akafufufuku amadziwa mitundu ya mbewu yomwe ilipo ndipo mtsogolo palibe amene angadzawabere luso kapena mbewuzo. Mndandanda woterewu umapatsa alimi kulimbika mtima kotu adzapitiriza kugwiritsa ntchito mbewu ndi luso lawo opanda munthu wina aliyense kuwaletsa, powauza kuti luso ndi mbewuzo ndi zake.

Izi zimathandizanso alimi kuchita kalondolondo wa kusintha kwina kullikonse komwe kumachitika ndi luso kapena mbewuzo, kuphatikizirapo kuyiwalika kwa nzeru zina za makolo. Luso ndi mbewuzo zimakhala poyera moti aliyense amaziwona m'minda ndi kuvomereza ntchito yayikulu yomwe alimi akugwira posunga ndi kuteteza luso ndi mbewuzo.

Mndandandawo utha kuthandizanso

pophunzitsa ana za mitundu ya mbewu ndi nzeru zomwe makolo awo akhala akugwiritsa ntchito m'deralo. Utha kuthandizanso boma pokonza malamulo ndi ndondomeko zina zothandiza kusamalira ndi kuteteza mbewuzo.

ZOKAMBIRANA

Konzani mndandanda wa mbewu za makolo zomwe zili m'dera lanu. Mndandandawo utha kuphatikiziraponso izi:

- Dera lomwe mtundu wa mbewuyo uli;
- Alimi omwe amalima mbewuyo;
- Kutalika kwa nthawi yomwe alimiwo asunga kapena kusamalira mbewuyo;
- Dzina la mbewuyo;
- Nthaka yomwe imachita bwino kapena kulola;
- Chikhalidwe cha mbewuyo (mawonekedwe, kukula ndi makomedwe ake);
- Ndi zisangalalo zotani zomwe anthu amakonda kudya mbewuzo;
- Mbiri ndi zikhulupiriro zokhudzana mbewuyo;
- Zokometsera zake;
- Masungidwe ake;
- Ntchito zina za mbewuyo (zitha kukhala ntchito zokhudzana ndi matenda omwe imathandiza ndi zina).

B. Malamulo a m'mudzi

Cholinga cha malamulo ndi kutsogolera magwiridwe a ntchito, komanso kulimbikitsa ubale pakati pa alimi omwe ndi ofunika kwambiri pa ntchito yosunga ndi kuteteza nzeru za makolo.

Awa ndi ena mwa malamulo omwe amathandiza alimi akumudzi kudziwa mmene angagwirire ntchito ndi anthu ochokera m'madera ena amene amafuna kudzapeza nawo nzeru, luntha, luso kapena mbewu zawo.

ZOKAMBIRANA

Kambiranani zomuyenereza munthu kugwiritsa nawo ntchito mbewu ndi nzeru zanu za makolo. Nanga mungateteze bwanji mbewu ndi nzeru zanu kuti anthu ena asakubereni?

C. Kusunga chikhalidwe ndi mayina a mbewu za makolo

Chilankhulo n'chofunika kwambiri poteteza ndi kusunga nzeru zomwe makolo athu akhala



Munda wochulukitsilamo mbewu ya mtedza pa Mkombezi Community Seed Bank.

akugwiritsa ntchito kwa zaka zambiri. Choncho ndi kofunika kupitiriza kugwiritsa ntchito mayina, upangiri, miyambo ndi zikhalidwe zomwe makolo akhala akuzitsatira pa ulimi.

ZOKAMBIRANA

Kambiranani chifukwa chiyani kuli kofunika kuteteza nzeru, luntha and zikhalidwe za makolo. Ndi nzeru, luntha kapena zikhalidwe zotani za makolo zomwe zili pachiopezo choyiwalika? Ndi zilankhulo ziti za makolo zomwe anthu akulankhulabe? Kodi chimachititsa n'chiyani kuti nzeru za makolo ziyambe kuyiwalika? Kodi ndi njira zotani zomwe zingathandize kuteteza nzeru za makolo?

Kumbukirani

Alimi ali ndi ufulu woteteza nzeru, luntha ndi zikhalidwe za makolo. Cholinga chotetezera nzeru ndi zikhalidwe za makolo ndi izi:

- (i) kuti zisayiwalike chifukwa mtundu uliwonse umadziwika bwino ndi zochita, komanso zikhalidwe zake;
- (ii) kuwopetsa anthu a mitundu ina

angazisokoneze. Kuteteza nzeru ndi zikhalidwe za makolo kumathandizanso kuti eni ake azitha kuzigwiritsa ntchito mosavuta.

5. Ufulu wa alimi wolandira phindu loyenera kuchokera ku mbewu zawo

Alimi ali ndi ufulu wopeza phindu kapena cholowa kuchokera ku mbewu zawo.

Ndibwino kuti alimi azindikire kuti phindu si ndalama zokha. Phindu litha kukhalanso mwayi wophunzira kuteteza ndi kugwiritsa bwino ntchito zachilengedwe za m'dera lawo. Kupeza nzeru zina zatsopano, luso la makono, upangiri wabwino ndi kumanga nawo mfundo za chitukuko kapena zaulimi - limenelonso ndi phindu.

Popeza nzeru ndi mbewu za makolo si za munthu mmodzi, koma ndi za mtundu wonse wa anthu a m'deralo, choncho aliyense ayenera kudyerera phindu lake. Mwachidule, mbewu za gulu ziyenera kupindulira gulu lonse osati mlimi mmodzi.

M'maiko mwina alimi adatsegula mabuku aku banki momwe amasungamo ndalama

zomwe amapeza kudzera mu kugulitsa mbewu ndi nzeru za makolo za m'deralo. Mwa zina, ndamalazo zimagwira ntchito yokonzera maphunziro a zaulimi, kumangira mabanki a mbewu akumudzi, kupereka ngongole kwa alimi zogulira zipangizo kapena kuwathandiza kukonza zokolola zawo. Umu ndi momwe maiko a anzathu akugwiritsira ntchito phindu lochokera mu nzeru kapena mbewu za makolo.

ZOKAMBIRANA

Santhulani ubwino womwe umapezeka kudzera mu kugulitsa mbewu ndi chakudya, pogwiritsa ntchito nzeru, luntha, upangiri ndi zikhalidwe za makolo.

Kumbukirani

Alimi ali ndi ufulu wopeza phindu kapena cholowa pogwiritsa ntchito mbewu, chakudya ndi nzeru za makolo awo. Phindu lake litha kukhala ndalama kapena zinthu zina zosiyaniyana.

MAGANIZO OTSIRIZA NDI MAVUTO OFUNIKA KUTHANA NAWO

Magulu ndi mabungwe osiyaniyana

akulimbikitsa alimi kudzera mu kafukufuku, zochitika ndi ndondomeko zina zambiri. Zochitikachitika zambiri ziyenera kugwirizana ndi malamulo ndi ndondomeko zaboma kuti zithe kukwaniritsa ufulu wa alimi mosavuta. Ena mwa mavuto ofunika kuthana nawo pofuna kupititsa patsogolo ufulu wa alimi ndi awa:

1. Kusanthula ndi kusintha malamulo a m'maiko okhudza kugulitsa, kusunga ndi kugwiritsa ntchito mbewu ndi zomera zina ndi cholinga choti zisatsutsane ndi ufulu wa alimi. China chofunika ndi kupeza njira zotetezera ndi kupititsira patsogolo mbewu za makolo ndi zamakono.
2. Kukhazikitsa malamulo othandiza kupititsa patsogolo ufulu wa alimi m'Malawi muno.

Munthu amene sadziwa za ufulu wake kumakhala kovuta kuti audyerere

MUTU WACHIWIRI

MALO OSUNGIRA MBEWU A KUMUDZI

Monga zafotokozedwa kale m'mutu woyamba, zina mwa ntchito ndi ubwino wokhala ndi malo osungira mbewu kumudzi ndi uwu:

- Kusunga mbewu zosiyanasiyana;
- Kubwezeretsa mbewu zoyiwalika;
- Kusunga mbewu ndi cholinga choti anthu akumudzi asadzavutike kuzipeza akadzazifuna mtsogolo;
- Sizivuta kusamala, komanso zimachita bwino ngakhale zitabzalidwa koposera kamodzi;
- Kusinthanitsa mbewu;
- Kupereka mbewu kwa alimi ovutika;
- Kuthandiza anthu ndi mbewu, komanso chakudya m'mudzi mukagwa ngozi zadzidzidzi;
- Alimi amapeza ndalama zothandizira mabanja awo akagulitsa mbewu zawo;
- Alimi amapeza mwayi wogawana upangiri ndi nzeru zina zokhudza ulimi ndi zachilengedwe;
- Kuluzanitsa ndi kuthandiza kusunga zachilengedwe zopezeka ndi zoyiwalika.



Nyumba yosungilamo mbewu ku dera la Mhuju, mudzi wa chikwawa mu boma la Rumphi

KUKHALA NDI MALO OSUNGIRA MBEWU M'MADERA A KUMUDZI KUMATHANDIZA KULIMBIKITSA UFULU WA ALIMI.

Ufulu wa alimi womwe uli pansu pa mgwirizano wa maiko wokhudza chakudya ndi ulimi wa International Treaty on Plant Genetic Resources for Food and Agriculture (ITPGRFA) ukuphatikizirapo:

- Kuteteza nzeru za makolo;
- Kuteteza, kugwiritsa ntchito, kusinthanitsa ndi kugulitsa mbewu;
- Kulimbikitsa alimi kupereka maganizo awo pa nkhani zokhudza mbewu ndi chakudya;
- Kupeza nawo phindu lochokera mu mbewu ndi chakudya.

ENI MALO OSUNGIRA MBEWU NDI MAGULU A ALIMI A KUMUDZI AKUKWANIRITSA UFULU WAWO MOTERE:

(a) *Kuteteza, kusunga ndi kugwiritsa ntchito mbewu;*

Malo osungira mbewu kumudzi amalimbikitsa alimi kuteteza ndi kugwiritsa ntchito moyenera mbewu za makolo, komanso za makono pofuna kuthana ndi njala m'madera mwawo.

Malowa amathandiza kubwezeretsa, kusunga ndi kuteteza mbewu m'midzi, komanso m'dziko; kuthandiza alimi kuti azipeza mbewu mosavuta; kulimbikitsa ulimi wachitsanzo kapena wabwino; komanso kuthandiza alimi kupeza ndalama zogulira zosowa zawo.

Malo osungira mbewu a kumudzi ndi wofunika kwambiri kaamba koti amapatsa mwayi alimi ang'onoang'ono wosunga mbewu m'mudzi mwawo momwemo ndipo akafuna kuzigwiritsa ntchito savutika kuyenda mtunda wautali.

(b) *Kusinthanitsa mbewu*

Malowa amalimbikitsa, komanso kuthandiza alimi kusinthana mbewu ndi luso.

Kafukufuku adawonetsa kuti malo osungira mbewu kumudzi amalimbikitsa alimi kuphunzitsana mmene angasungire mbewu potsata njira zosiyanasiyana kuphatikizirapo za makolo, komanso mmene angazigwiritsire ntchito kuphatikizirapo kupanga mankhwala osiyanasiyana.

(c) *Alimi anzawo kuti awathandize mbewu, komanso upangiri wabwino*

Alimi—kudzera m'malo osungira mbewu kumudzi— amapempha chilolezo kuchokera kwa anzawo kuti agwiritse nawo ntchito mbewu, njira kapena upangiri wawo wa ulimi mogwirizana ndi malamulo a gululo, komanso aboma okhudza kugawana zinthu ndi phindu lochokera mu ulimi.

(d) *Kusankha mbewu yogulitsa*

Malo osungira mbewu kumudzi amakhala ndi mphamvu zosankha, komanso kugulitsa mbewu. Dziko la Brazil lidakhazikitsa kale malamulo omwe amapatsa mphamvu mabankiwa kusunga ndi kugulitsa mbewu opanda kupempha chilolezo ku boma kapena ku bungwe lililonse.

(e) *Kuteteza nzeru za makolo*

Kupatula kusunga mbewu, malowa amalimbikitsanso alimi kuteteza upangiri, nzeru ndi njira zosiyanasiyana za ulimi zomwe makolo akhala akugwiritsa ntchito kwa zaka zambiri.

(f) *Kulimbikitsa magulu, mabungwe ndi kuthekera kwa alimi*

Malo osungira mbewu a kumudzi amakhazikitsidwa ndi alimi omwe amapanga malamulo a momwe mabankiwa ayenera kuyendera. Izi zimalimbikitsa magulu ndi mabungwe a alimi makamaka pokhazikitsa malamulo akayendetsedwe ka maguluwo, kulemba mndandanda zinthu, kalondolondo wa zochitika ndi mmene malowa akusinthira miyoyo ya alimi.

ZOTI ATSOGOLERI ATSATE POKHAZIKITSA KAPENA KUTHANDIZA MALO OSUNGIRA MBEWU KUMUDZI

Kusamalira malo osungira mbewu kumudzi ndi kukhazikitsa ena atsopano kumalira zambiri monga kusonkhanitsa, kusankha ndi kugawa mbewu; zipangizo ndi matumba osungiramo mbewu akhale osamalika ndi owuma bwino. Malo osungira mbewu a kumudzi ayenera kulandira thandizo kuchokera kwa maboma ndi maunduna osati mabungwe okha omwe amapereka ndalama ndi upangiri osiyanasiyana. Ndondomeko ya mbewu (National Seed Policy) yomwe boma likukonza liyenera kupereka dongosolo la kakhazikitsidwa ndi kayendetsedwe ka malo osungira mbewu kumudzi.



Kusunga kwa mbewu mkati mwa nyumba yosungira mbewu ku mudzi wa chikwawa, mdera la Mhuju mu boma la Rumphu

Atsogoleri ayenera kudziwa kufunika kwa malo osungira mbewu kumudzi ndi kulimbikitsa anthu kuwakhazikitsa m'madera mwawo ndi cholinga choti azisungamo mbewu ndi chakudya. Ayeneranso kuwonetsetsanso kuti malowa akuyenda bwino, komanso kukwaniritsa ntchito yawo.

Atsogoleri ayenera kugwirana manja ndi alimi ang'onoang'ono ndi kulimbikitsa ntchito yosunga mbewu, kuthana ndi njala ndi kutsatira ulimi wosamalira zachilengedwe.

Ndi zofunika kuti atsogoleri aziyendera malo osungira mbewu akumudzi kuti azikadziwonera mmene akuthandizira alimi kusunga mbewu, chakudya, komanso kulimbana ndi njala.

Atsogoleri, akuluakulu akafukufuku, mabungwe ndi maiko omwe amapereka thandizo akavomereza kuti mabankiwa ndi wofunika, alimi adzalimbikitsika ndipo ntchito za malo osungira mbewu akumudzi zidzapita patsogolo.

Malo osungirako mbewu a Malawi Plant Genetic Resources Centre (MPGRC) ku Chitedze ku Lilongwe akuthandiza mabungwe osiyanasiyana monga la Biodiversity Conservation Institute (BCI) kukhazikitsa malo osungira mbewu m'madera a kumudzi. MPGRC yakhala ikuphunziisa ogwira ntchito ku BCI luso la kasungidwe ka mbewu. Mamembala a CSB adakachezanso ku

MPGRC ku Chitedze kukaphunzira kapangidwe, kasamalidwe, kagawidwe ndi kuchita kalondolondo wa mbewu.

Alimi adapindula kwambiri atakacheza ku maofesi a bungwe la International Crops Research Institute for the Semi-Arid Tropics (ICRISAT) omwe ali ku malo azakafukufuku a Chitedze. Mwa zina, alimi adawona mmene anzawo amakonzero ndi kusamalira mbewu ya mtedza ndi nandolo. Alimi a m'derali ali pa mgwirizano wochulukitsa mbewu ndi bungwe la ICRISAT. Alimi 16 omwe ndi mamembala a gulu la Mkombezi adapeza mwayi wochulukitsa mtedza m'munda wa mahekita khumi (10). Alimiwa akuyembekezera kupha makwacha kudzero mu ntchitoyi.

ZOKAMBIRANA

1. Zindikirani ndipo kambiranani phindu la malo osungira mbewu kumudzi kwa alimi;
2. Tchulani njira zothandiza kuti malo osungira mbewu kumudzi akhazikike;
3. Fotokozani zomwe anthu angachite polimbikitsa kapena pofuna kuthandiza malo osungira mbewu a kumudzi;
4. Fotokozani zinthu zingapo zothandiza kuzindikiritsa anthu kufunika kokhazikitsa malo osungira mbewu m'madera a kumudzi ngati ndondomeko ya m'dziko lino la Malawi.

MUTU WACHITATU

UFULU WA ALIMI ACHIZIMAYI

Mwa alimi 100 aliwonse omwe ali m'dziko lino la Malawi, 70 ndi achizimayi ndipo mwa magawo 100 aliwonse a chakudya chomwe mabanja awo amapeza, 80 amabweretsa ndi amayiwa. Amayiwa ndiwo amasunga njira, upangiri ndi nzeru zomwe makolo akhala akugwiritsa ntchito kwa zaka zambiri zomwe ndi zofunika kwambiri potukula ulimi, komanso kuthetsa njala.

Nthawi yafika yoti maiko azindikire ntchito yayikulu yomwe alimi achizimayi akugwira ndi kuyamba kuteteza ufulu wawo.

Mkulu wa amayi m'bungwe la United Nations, a Phumzile Mlambo-Ngcuka, adalankhula motere: "Tiyenera kulimbikitsa ndi kuteteza ufulu wa amayi akumudzi. Amayi akakhala ndi malo olima, mabanja achita bwino, zokolola zichuluka ndipo tsankho limachepa. Ndipo nkhondo yolimbana ndi umphawi, nkhanza ndi matenda a HIV ndi Edzi imayenda bwino. Moyo wa aliyense umapita patsogolo."

Kuzindikira ntchito yayikulu yomwe amayi amagwira paulimi kuthandiza kuthetsa kusiyana pa ntchito zomwe amayi ndi abambo amagwira pa ulimi; komanso amayi akaphunzitsidwa bwino za maifulu awo amakhala ndi chidwi chowumenyera, kuwukwaniritsa ndi kuwudyerera.

Cholinga cha mutu uwu ndi kuwonetsera ntchito yayikulu yomwe alimi achizimayi amagwira pothandiza kupeza chakudya cha mabanja awo, kuthetsa njala, komanso kupeza njira zothandiza kuti alimi achizimayi akwaniritse ndi kudyerera maifulu awo.

UDINDO WA AMAYI PA ULIMI

Ngakhale mwa alimi 100 aliwonse, 70 ndi amayi; mwa magawo 100 aliwonse a chakudya cha pakhomu, amayi amapeza 80 - amayi ambiri alibe mphamvu pa zokolola zawo, komanso sapindula ndi ndalama zomwe zimapezeka mu ulimi. Mwayi ndi mphamvu za amayi pa ulimi n'zochepa kwambiri moti ambiri amavutika kupeza

ulangizi, mauthenga, zipangizo, ngongole, malo wolima ndi zinthu zina zosiyanasiyana zochitira ndi kupititsira patsogolo ulimi wawo. Izi zimalepheretsa kuthekera kwawo kotukula ndi kuchita ulimi wokhazikika, komanso wosamalira zachilengedwe.



Mlimi kuonetsa mbewu yake yomwe anasunga kukonzekera nyengo yolima yotsatira.



Mlimi wamkazi wakuwonetsa ndikulongsolera Mafumu za ulimi wamapira pa Chikwawa Community Seed Bank.

Kupatula kugwira ntchito yochuluka, tsankho pakati pa amayi ndi abambo pakapezedwe ka zipangizo za ulimi limalepheretsa amayi ambiri kuchita ulimi waphindu. Amayi amavutika kupeza misika ya mbewu zawo kaamba ka vuto la mayendedwe, kusowa kwa njira zabwino zochitira malonda, komanso luntha lonenerera mitengo yabwino ndi ogula. Abambo amatenga gawo lalikulu pa malonda zomwe zimawapatsa mwayi wochita bwino pa chuma poyerekeza ndi amayi.

Mwa mabanja 100 aliwose a m'dziko muno, 30 amatsogozedwa ndi amayi. M'mabanja ena, abambo amagwira ntchito zina n'kusiya ulimi m'manja mwa amayi.

M'madera ena momwe anthu amakhulupirira kuti wamkulu pabanja ndi mwamuna, ntchito zobweretsa chakudya ndi ndalama zomwe amayi amagwira saziwerenga popeza amayi amawatenga kuti ndiwongothandizira abambo. Maganizo woti ulimi ndi ntchito ya abambo akuchititsa kuti amayi azikumana

ndi zipsinjo zosiyanasiyana, komanso asachite bwino pa ulimi.

Amayi amapeza malo wolima kudzera m'mabanja. Izi zikutanthauza kuti banja likatha kapena mwamuna kumwalira, mwayi wa mayi wokhala ndi malo umatheranso pomwepo. Mwamuna akamwalira, abale ake amalanda munda kaamba koti anthu ambiri safuna mayi azikhala ndi malo akeake wolima. M'dziko muno munthu amapeza malo kuchokera ku mtundu kapena ku mbumba yawo. Mwachitsanzo, m'maboma ambiri a m'chigawo chakummwera ndi pakati, mbumba imadzera mwa mayi pamene m'chigawo cha kumpoto imadzera mwa bambo. Eni mtundu kapena mbumba, amakhala ndi mphamvu komanso mwayi wa malo pamene anzawo apabanjawa sapeza nawo mwayi wa malo. Magawo awiri mwa magawo atatu achiwerengero cha anthu a m'dziko lino la Malawi mbumba yawo imachokera kwa amayi omwe amakhala ndi malo ngati cholowa chawo. Ngakhale mayi ali

mwini malo, mphamvu yoyang'anira malowo imakhala ya kwa atsibweni ochokera m'banja la amayi ake. Zotsatira zake amayi sakhala ndi ulamuliro, mphamvu zopereka maganizo awo pa kayendetsedwe ndi kagwiritsidwe ntchito ka malo.

Amayi amapatsidwa mwayi wobzala mbewu za mtundu wa nyemba, mtedza, mbatata ndi chinangwa. Vuto la mbewuzi ndi loti sachita nazo bwino kwambiri pa chuma kaamba koti chimanga-chomwe alibe nacho mphamvu ndi chomwe anthu amadalira pa chakudya.



28

Alimi aakazi kusankha mbewu yoti adzadzale nyengo yodzala mbewu ikadzakwana.



Mlimi wamkazi waku Bulala, Find Your Feet, kuonetsa mawere amene anakolora.



Alimi aakazi aku Hewe, Find Your Feet, Kuonetsa kukondwa pokolora chimanga.

Pofuna kuzindikira udindo wa amayi ndi kuwapatsa mphamvu pa ulimi, boma la Malawi mogwirizana ndi mabungwe osiyanasiyana omwe si aboma adakonza mapologalamu omwe cholinga chake ndi kuthandiza amayi kupeza zipangizo za ulimi, ngongole ndi ulangizi mosavuta, komanso kulimbikitsa kuthekera kwawo kudzera m'maphunziro.

Malawi ndi limodzi mwa maiko osauka kwambiri pa dziko lonse. Malingana ndi lipoti la za chitukuko la Human Development Report lomwe lidatuluka m'chaka cha 2013, mwa maiko 186, Malawi ili pa 171 pa nkhani ya umphawi.

Pachifukwa ichi, boma ndi mabungwe ayenera kugwirana manja ndi cholinga chofuna kuthana ndi malamulo atsankho omwe akhala akupondereza amayi pa chuma, pa nkhani yopeza malo, zipangizo za ulimi mosavuta, kuwapatsa mwayi wofanana ndi abambo, komanso kuwathandiza kutukuka pa ulimi.

Buku loona kusiyana pakati pa abambo ndi amayi lotchedwa Gender in Agriculture Source Book likufotokozza mwatsatanetsatane ndi kupereka zina mwa njira zomwe zili m'munsimu kuti zithandize kulimbikitsa ufulu wa alimi achizimayi:

A. Ulamuliro wabwino umathandiza alimi achizimayi kutenga gawo pomanga mfundo ndi kupereka maganizo awo momasuka

Ulamuliro wabwino, malingana ndi tanthauzo la bungwe la United Nations (UN), ndi kutengapo gawo pazochitika, kuchita zinthu poyera, kukhala mdindo wabwino, kugwirizana zochita ndi kutsata malamulo.

Ngakhale amayi akugwira ntchito yayikulu yokonza ndi kusunga chakudya, ndondomeko zambiri za ulimi zimatofotoza molakwitsa kuti alimi, komanso ogwira ntchito ambiri omwe ali m'madera akumudzi ndi abambo.

N'chifukwa chake n'koyenera kukonza ndondomeko za ulimi zounikira bwino ntchito zomwe abambo ndi amayi amagwira, kupereka mphamvu kwa amayi zoti azitenga nawo gawo pa zokambirana, komanso kupatsa amayi mwayi wofana ndi wa abambo. Kuphatikizira apo, n'kofunika kukhazikitsa mfundo zothandiza amayi kukonza nawo ndondomeko ndi mfundo zokhudza ulimi.

Maphunziro ndi kuzindikiritsa amayi za ufulu wawo ndi zothandiza kuti azitenga nawo gawo pokonza ndondomeko za ulimi. Nawo abambo ndiwofunika maphunziro kuti azindikire ntchito yayikulu yomwe amayi amagwira.

Ngakhale ndondomeko zabwino ndi zofunika, pazokha ndi zosakwanira kuthana ndi mavuto omwe amayi amakumana nawo. Maunduna ndi madipatimenti aboma akufunika kukhazikitsa ndondomeko ndi mapulogalamu wotheza tsankho lomwe lili pakati pa abambo ndi amayi.

Thandizo loyenera litha kusintha maganizidwe a anthu akumudzi, kulimbikitsa kufala kwa mauthenga, komanso kuthandiza kuti amayi ndi abambo azigawana mauidindo mofanana. Malamulo apadera oti amayi ndi abambo azigawana mauidindo mofanana athanso kuthandiza kuthetsa tsankho pakati pawo.

B. Kupeza zipangizo zamakono, zachilengedwe, ndalama ndi misika

Podziwa mmene misika imayendera, kuzindikira zofuna za ogula ndi nthawi yoyenera kugulitsa zokolola, alimi a akazi adzachita bwino pa malonda.

Mapulani abwino atha kuthandiza alimi achizimayi kupeza mbewu zabwino kudzera mu ziwonetsero za ulimi ndi ndondomeko zina zomwe boma ndi mabungwe amakhazikitsa pofuna kulimbana ndi njala.

Pofuna kusintha zinthu, mabungwe omwe amapereka thandiza la ulimi aziwonetsetsa kuti ayika padera ndalama zothandizira alimi achizimayi, komanso m'misonkhano yawo alimi achizimayi akuyimiridwa mokwanira ndipo maganizo awo akugwiritsidwa ntchito.



Mlimi kufotokozera mbewu zake kwa anthu oonerele ku Chionetsero chachikulu chazamalimidzwe ku Blantyre, Malawi.

C. Kulimbikitsa amayi kupanga magulu akumudzi

Kukhala m'magulu kumapindulira amayi popeza amapeza mwayi wa ngongole za ndalama, mbewu, fetereza ndi katundu wina wambiri, komanso kumawapatsa mphamvu zopereka maganizo awo ndi kuwathandiza kumanga mfundo zokhudza

miyoyo yawo. Magulu akumudzi a amayi amawathandizanso kupeza katundu wa gulu mosavuta, kusunga mbewu, luso ndi nzeru za makolo. Magulu amadzetsa chimvano pakati pa amayi, kuwapatsa mtima wodzikhulupirira ndi kuwathandiza kuti azidziwika ngati gulu osati mlimi aliyense payekhapayekha.



Mamembala a Chikwawa Seed Bank kugwira ntchito limodzi posunga mbewu pagulu.

D. Kulimbikitsa kuthekera kwa amayi

Kudzikhulupirira ndi kuphunzitsa amayi utsogoleri kutha kuthandiza kuti akhale ochitachita, komanso azipeza nawo phindu pa zochitikachitika za m'madera awo. Amayi omwe sadaphunzire mokwanira amavutika kutenga nawo gawo pa zokambirana kaamba koti zambiri zimakhala zolembedwa. Choncho amayi ayenera kuphunzira mokwanira momwe utsogoleri, ndondomeko zosiyanasiyana ndi magulu amayendera.

E. Kudziwitsa anthu

Alimi achizimayi ayenera kuzindikira za ufulu wawo kuti azitha kuufunsa, kuukwaniritsa m'madera ndi m'maiko mwawo.

F. Kupititsa patsogolo ndi kuteteza nzeru za makolo

M'midzi amayi ndiwo amapititsa patsogolo ndi kusunga nzeru za makolo zokhudza kachitidwe ndi kagwiritsidwe ntchito ka zinthu zosiyanasiyana. Ntchito yosankha, kusamala ndi kusunga mbewu pakati pa alimi ang'onoang'ono imakhala ya amayi. Amayi alinso ndi luso lozama pa nkhani yobzala mbewu zothandiza kuchiza matenda, yosamalira minda ing'onoing'ono ya pakhomo, komanso kupeza chakudya cha anthu a pa pabanja pawo, komanso cha ziweeto.

ZOKAMBIRANA

Kambiranani ndi kuyankha mafunso otsatirawa:

1. Kodi alimi achizimayi a m'dera mwanu amathandiza motani kutukula ulimi?
2. Tchulani zinthu zomwe zimabwezera mmbuyo ufulu wa alimi achizimayi. Nanga ndi njira zotani zomwe zingathandize kuthana ndi mavutowa?
3. Kodi n'kofunika bwanji kuti amayi a m'dera, komanso m'dziko muno azipereka maganizo awo pakayendetsedwe ka ntchito zaulimi?
4. Kodi ufulu wa alimi achizimayi ungapite bwanji patsogolo? Tchulani mfundo zomwe zingathandize kukwaniritsa izi.
5. Kodi chilungamo pa ndondomeko za mbewu ndi malamulo a za ulimi zingathandize bwanji kulimbikitsa kusamalira zachilengedwe, ulimi komanso ufulu wa alimi achizimayi?



Norad

